

YANKHULANANI KAYE NDI MADELA OKHUDZIDWA!

M'MABOMA A DEDZA NDI LILONGWE, MALAWI,
NTCHITO YA CHITUKUKO IKUYIKA PA CHIWOPSYEZ
MAKOMO KOMANSO ZINTHU ZODALIRIKA
PA UMOYO WA ANTHU OPOSA 5,100.

DAMU LA DIAMPHWE


NDI MBALI IMODZI YA
NDALAMA ZOKWANIRA
\$ 290 MILIYONI

ZOCHOKELA KU WORLD BANK, EUROPEAN INVESTMENT BANK,
AFRICAN DEVELOPMENT BANK KOMANSO BOMA LA MALAWI.

MALO A MA HEKITALA

2,682 OGWIRITSIDWA NTCHITO NDI MIDZI YOZUNGULIRA
SADZATHANSO KUWAGWIRITSA NTCHITO,

ZIMENEZI ZIZAPHWANYA UFULU WA ANTHU OKHUDZIDWAWO.



MALAWI
Lilongwe

- KUONONGEKA KWA MINDA
- KUONONGEKA KWA NYUMBA
- KONONGEKA KWA MISIKA, MASUKULU, MANDA
- KUKHUDZIDWA KWAKUKULU KWA CHILENGEDWE,
MALO ACHILENGEDWE KOMANSO NYAMA ZAKUTHENG
- KUONONGEKA KWA MALO A CHIKHALIDWE NDI MBIRI
- ZINTHU ZOKHUDZIDWA NDI CHITUKUKOCHI


Mabungwe a International Accountability Project ndi Citizens for Justice (CFJ) anakonza kawuniwuni ndi anthu okhudzidwa mu maboma awiriwa.

IZI NDI ZIMENE ADANENA

Pafupifupi anthu onse
sadafunsidwepo
zamaganizo awo pa
nthawi yopanga
mapulani a chitukukochi

Anthu nayini pa
anthu teni aliwonse
adadziwa za
chitukukochi
mapulani onse
atamatilizidwa kale

Pafupifupi anthu eyiti pa
anthu teni aliwonse
sankadziwa chilichonse za
chitukukochi kuti athe
kupereka maganizo awo pa
mapulani a chitukukochi



Anthu oposera
anayi pa anthu teni
aliwonse sanali
omasuka kukamba
zakukhosi kwavo

Anthu nayini pa anthu
teni aliwonse akuganiza
kuti maganizo awo
sadagwiritsidwe ntchito
mu mapulani a
chitukukochi

Pafupifupi anthu onse
sankadziwa za World
Bank ndi zokhudza
malamulo awo
ogwirira ntchito

YANKHULANANI NDI ANTHU
OKHUDZIDWA MUSANAYAMBE
CHILICHONSE CHOKHUDZA CHITUKUKO

PEREKANI UTHENGA OYENERA
KUTI KUYANKHULANA NDI ANTHU
A M'MADERA ZIKHALE ZOPINDURA

“ Anthu a m'madera akuyenera
kufunsidwa maganizo awo ndi
cholinga chothana ndi mantha
komanso nkawa zavo.”

“ Tinawuzidwa kuti tinalibe
mwaiyi wokana chitukukochi
ngakhale anthu ena samakondwera nacho.”

PEREKANI MIYAYI YAKUTI ANTHU
OKHUDZIDWA NDI CHITUKUKO ASANKHE
PA ZOKHUDZANA KUWASAMUTSA

“ Tikukakamizidwa kusamuka.
Chitukukochi chingakhale
bwani chaphindu kwa ife?
Ngati akuti kusamuka ndi
koyenera, akuyenera
kutipezera malo komanso
kutimangira nyumba
zokhalamo.”

CHILI KUTSOGOLO
NDI CHIYANI?

Kugwiritsa ntchito zotsatira
za kawuniwuniyu, midziyi
ikudziwitsa anthu
amawudindo za chitukuko
chimene akufuna.